Baibulo ya ana

Ikupasilani

Kubadwa kwa Yesu



Yolembedwa ndi: Edward Hughes
Yojambulidwa ndi: M. Maillot
Yotengedwa ndi: E. Frischbutter; Sarah S.
Yotathauzidwa ndi: Phiri Williams
Yo pangidwa ndi: Bible for Children
www.M1914.org

BFC
PO Box 3
Winnipeg, MB R3C 2G1
Canada

©2013 Bible for Children, Inc.
Chilolezo: Muli ndi ufulu wotenga ndi kuchurukitsa makopewa koma osagulitsa.

Nthawi yakale, Mulungu anatumiza mngelo Gabriyeli kwa mzimai wokongola wa chiyuda dzina lake Maria. Anamuuza kuti, "uzakhala ndi mwana ndipo mudzamucha dzina lake Yesu. Adzachedwa mwana wa wam'mwamba mwamba. Adzalamulira kwamuyaya."



“Kodi zimenezi zizachitika bwanji?”
mtsikana wodabwitsa yu anafunsa.
“Ineyo sindinakhalepo ndi
mwamuna aliyense.”
Mngelo anamuuza
Maria kuti
mwanayo
adzachokera
kwa Mulungu.
Sadzakhala ndi
tate wa kuthupi.



Kenaka mngelo anamuuza Maria kuti msiweni wako Elizabeti ali ndi mwana muukalamba wake. Ndipo ichi chinali chozizwa. Kenaka Maria anamuyendera Elizabeti. Anamu lemekeza Mulungu limodzi.

Ndipo Maria anazipereka kwa mwamuna wake Yosefe. Yosefe sanakondwele pamene anamva kuti Maria aliwoyembekedzera. Iye anaganiza kuti ndiya abambo ena.

Mmaloto, mngelo wa Mulungu anamuuza Yosefe kuti mwanayu ndimwana wa Mulungu. Yosefe anali woti athandize Maria kuyanganira mwanayu.

Yosefe anadalira ndiku mvera Mulungu. Ndiponso anamvera malamulo adziko lawo. Chifukwa cha malamulo atsopano, iye ndi Maria anasiya mzinda wa kwao,

Betelehemu, kukapereka msonkho.

Ndipo Maria anali wokhonzeka kukhala ndi mwana. Koma Yosefe sanathe kupeza chipinda kulikonse. Malo aalendo onse anali odzadza.

Pomaliza penipeni Yosefe anapeza khola la n'gombe. Mmenemo, Yesu anabadwira. Amai wake anamugoneka mkholamo, pamalo pamene anayikapo zakudya za n'gombe.

Pafupi pake azibusa anagona poyanganira n'gombe zawo. Mungelo wa Mulungu anawonekera ndikuwauza uthenga wabwino.

“Kwabadwa mwana kwa inu tsiku la lero mumdzinda wa Davide mpulumutsi amene ndi Yesu Kristu.

Muzampeza mwanayu atagona mkhola.”

Mwadzidzidzi, angelo ambiri owala anawonekela, ndikumulemekeza Mulungu nati, ...



... “Ulemelero kwa Mulungu wammwamba
mmwamba ndi mtendere padziko lapansi,
ndichifuniro chabwino kwa anthu
onse apadziko lapansi.”

Ndipo azibusa anafulumira kupita ku khola. Atatha kumuwona mwanayo anawuza wina aliyense anakumana naye zimene mngelo adanena za Yesu.



Patapita masiku makhumi anayi,
Yosefe ndi Maria anambweretsa
Yesu kukachisi ku
Jerusalemu.
Kumeneko munthu
ochedwa Simioni
analemekeza
Mulungu chifukwa
cha mwana,
pomwe Anna
okalamba, mtumiki
wina wa Ambuye,
anathokoza.



Wonse amaziwa kuti Yesu ndi mwana wa Mulungu, mpulumutsi wolonjezedwa uja. Yosefe anapeleka nsembe mbalame ziwiri. Iri ndilo lamulo ya Mulungu yoti osauka akufunika atabweretsa chopereka pokamuwonetsa mwana atabadwa kwa Ambuye.

Patapita nthawi,
anzeru akummawa
anatsogoleredwa
ndi nyenyezi
kuchokera
kummawa kwa dziko lawo
kupita ku Jerusamu. “Alikuti
wobadwayo mfumu ya Ayuda?”
anafunsa. “Tikufuna
timulambire iye.”

Mfumu Herodi anamva za anzeru akummawa. Anabvutika, nawafunsa iwo kumene angathe kukampeza ndipo amuuze akampeza Yesu. Herodi anati, "Ndifuna inenso ndikamulambire iye." Koma amanama. Herodi amafuna kumupha Yesu.

Ndipo nyenyezi inawa tsogolera anzeru akummawa ku nyumba yeni yeni komwe Maria ndi Yosefe anakhala ndi mwana wamn'gono uja. Namlambira pogwada, azamalonda anapereka mphatso za golide ndi mafuta onunkhiritsa.

Mulungu anawachenjedza anzeru akummawa kuti abwelere kumuzi mwakachetechete. Herodi anakwiya.

Anafunitsitsa kuwononga Yesu, ndipo wolamurira woipayu anapha ana amuna achichepere mu Beterehemu.



Koma Herodi sanakhonze kupha mwana wa Mulungu! Anachenjezedwa ku maloto, Yosefe anatengera iye Maria ndi Yesu kuthawira ku Iguputo.

Pamene Herodi anamwalira Yosefe anatenga Maria ndi Yesu kubwelera kuchoka

ku Iguputo.
Anakhala kumzinda waun'gono
ku Nazareti, pafupi ndi Nyanja ya Galileya.

Kubadwa kwa Yesu

Nthano yochokera mu mau a Mulungu, Baibulo,

opezeka mu

Mateyu 1-2, Luka 1-2

“Polowela pa mau anu pamapasa kuwala.”
Masalimo 119:130

Mapeto

Nthano iyi yamBaibulo imakamba za ubwino wa Mulungu yemwe anatipanga ndipo akufuna kuti mumdziwe iye.

Mulungu amadziwa kuti tima chita zoipa, zimene zimachedwa chimo. Chilango cha uchimo ndi infa, koma Mulungu anatikonda kwambiri ndipo anatuma mwana wake yekha, Yesu, kuzatifela pamtanda ndi kunzunzika chifukwa cha machimo anu. Ndipo anaukanso kwa akufa na pita kumwamba! Ngati ukukhulupirira Yesu mupempheni akukhululukileni machimo anu, azakukhululukirani! Adzabwera kukhala nanu, ndipo muzakhala naye kunthawi zonse.

Ngati mukukhulupirira kuti izi ndizoona, nenani ichi kwa Mulungu: Ambuye Yesu, ndikhulupirira ndinu mwana wa Mulungu, ndipo munakhala munthu kundifera ine machimo yanga, ndipo mulinso ndi moyo. Chonde, lowani mmoyo mwanga ndikundi khululukira machimo anga, kuti ndikhale ndi moyo watsopano, ndipo tsiku lina ndikakhale ndiinu muyaya. Ndithandizeni kukumverani ndi kukhala mwa inu ngati mwana wanu. Ameni.

Welenga Baibulo ndi kuyankula ndi Mulungu matsiku onse!
Johane 3:16